

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

TSIKU LA AMBUYE

Yohane, wophunzira wokondedwa uja, anali atasiyidwa pa chisumbu cha Patmo pamene analemba kuti, “Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mau akulu, ngati a lipenga” (Chivumbulutso 1:10). Chivumbulutso chimenechi chinaperekedwa kwa Yohane pa nyengo iyi ya mtengo wapatali. “Tsiku la Ambuye” limatchedwanso kuti tsiku loyamba la sabata, kapenanso Lamulungu.

Loweruka, limene linali tsiku lomaliza la sabata, linali ndi tanthauzo lapadera kwa Ayuda amene anali pansi pa chilamulo chakale ndipo anali omangidwa ndi lamulo losunga Sabata kukhala tsiku lopatulika, lopumula komanso lopembedza. Atabwera Yesu Khristu, Akhristu sakhalanso pansi pa Lamulo ndipo salamulidwanso ndi zolamulira zake. Akhristu oyamba anapanga mwambo watsopano womasonkhana pofuna kupembedza pa tsiku loyamba la Sabata ndipo iwo analitcha kuti “Tsiku la Ambuye”.

Tsiku Lamulungu nalonso linali ndi tanthauzo lapadera kwa okhulupirira popeza kuchokera pamene Ambuye Yesu anakhomedwa pamtanda, ndi pa tsiku loyamba la Sabata pomwe Ambuyewo anaukitsidwa m'manda. “Koma tsiku loyamba la sabata, mbandakucha, anadza kumanda Ndipo anapeza mwala unakunkhunizidwa kuuchotsa pamanda. Ndipo m'mene analowa sanapeze mtembo wa Ambuye Yesu” (Luka 24:1-3).


Lamulungu linapitirira kukhala lofunikira monga tsiku lapadera chifukwa Mzimu Woyera

anaperekedwa kwa Akhristu okhulupirira pa tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:1-4) ndipo izi zinachitika pa tsiku loyamba la Sabata. Chikondwerero cha Masabata, kapena tinene kuti Pentekoste, chinali chikondwerero cha zokolola zakumunda chimene malingana ndi malamulo a Chiyuda amakumbukiranso kuperekedwa kwa Malamulo pa Phiri la Sinai. Chikondwererochi chimachitika patatha masiku 50 kuchokera pa Pasaka. Pali kufananiza kosangalatsa. Khristu anakhomedwa pamtanda chifukwa cha machimo a anthu pa nthawi ya Pasaka. Kutsatira apa, pa Pentekoste Mzimu Woyera anatsika ndipo analemba Lamulo lakumwamba la Mulungu m'mitima mwa anthu okhulupirira.

Potengera zifukwa izi, ndikomveka ndithu chifukwa chimene otsatira a Khristu anayamba kupembedza Lamulungu m'malo mwa Loweruka. Iwo samamangika kuti adzisunga Sabata ndipo tsiku loyamba la sabata linali ndi tanthauzo lalikulu komanso lofunikira kwa iwo.

Malingana ndi Malemba, mpingo woyamba ukuoneka kuti umapembedza pa tsiku Lamulungu. “Ndipo tsiku loyamba la sabata, posonkhana ife kunyema mkate, Paulo anawafotokozera mau, popeza anati achoke m'mawa mwake; ndipo ananena chinenera kufikira pakati pa usiku.” (Machitidwe 20:7). Paulo analangiza oyera mtima mu I Akorinto 16:1-2 kuti, “Koma za chopereka cha kwa oyera

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Tsiku Lamulungu linali ndi tanthauzo lapadera kwa okhulupirira popeza ndi pa tsiku loyamba la Sabata pamene Ambuye Yesu anaukitsidwa m'manda ...”

Mawu a Mkonzi

3

Kusanthula Mau a Mulungu: Sabata

4

Nkhani Yotsagana Nayo: Sabata la Mose ndi Sabata la Chikhristu

5

Mafunso ndi Mayankho

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

mtima, monga ndinalangiza Mipingo ya ku Galatiya, motero chitani inunso. *Tsiku* loyamba la sabata yense wa inu asunge yekha, monga momwe anapindula, kuti zopereka zisachitike pakudza ine.” Zopereka zao zimasonkhanitsidwa pamodzi pa tsiku Lamulungu kusiyana ndi tsiku lakale la Sabata ndipo panali ndondomeko yotsatirika bwino yakuti oyera mtima anali kukumana ndi kupembedza Lamulungu.

Kuchokera pa nthawi ya Khristu, pakhala pakuchitika mwambo pakati pa mpingo wachikhristu wakupatula Lamulungu, limene lili Tsiku la Ambuye, kukhala tsiku limene anthu adzipatula nthawi napembedza pamodzi. Ngakhale palibe lamulo m’malemba za ichi, monga m’mene zinaliri ndi kusunga Sabata mu Chipangano Chakale, Malemba amatiphunzitsa kuti tisaleke kusunkhana pamodzi kwa okhulupirira (Ahebri 10:25).

Palibepo cholakwika ndi kukumana pamodzi ndi kupembedza pa tsiku lina lililonse kupatula Lamulungu, koma pali cholakwika choonekeratu ndithu ndi mpingo imene imakumana tsiku Loweruka ngati njira yofuna kusunga Sabata. Iwo akugwiritsitsa Lamulo limene linapita ndi mulibe chilungamo mu tsikuli. Pofuna kusunga chikhalidwe chakunja cha Lamulo, iwo amasemphana ndi choonadi chachikulu cha ufulu komanso chilungamo chenicheni zimene zili mwa Yesu Khristu.

Ngakhale Akhristu ena akhoza kumakumana masiku ena Sabata pofuna kukwaniritsa malamulo a dziko limene akukhalamo kapena malingana ndi kuti Sabata ndi tsiku logwira ntchito, monga m’mene zimachitikira m’maiko ena Achisilamu, nawonso akhoza kuwona ubwino ndi ufulu wa Tsiku la Ambuye pa tsiku lililonse la Sabata. —mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m’dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonza za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo ku-matithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.org. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m’maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulanso mwini wake kuntchito zake, monganso Mulungu kuzake za Iye. —Ahebri 4:9-10

Mpumulo wa mzimu umene uli mwa Yesu ndi wa ulemmerero woposa. Kudzera mwa Yesu Khristu, pali mtendere umene umapambana chidziwitso chonse. Uwo umaposa mavuto ndi namondwe wa moyo uno ndipo uchita mizu ndi kukhazikika mu mtima mwa mwana wa Mulungu.

Umenewu sumachokera ku ntchito zathu kapena ku chilungamo chathu, koma ku kupezeka kwa Mwana wa Mulungu pakati pathu.

Ulendo uno tipitirira kutsatira pa maziko amene tidamanga mu Kalata ya No. 18 okhudzana ndi mapangano amene Mulungu anapanga ndi mtundu wa anthu. Kusunga tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika ndi limodzi la Malamulo Khumi mu Chipangano Chakale. Ili linali limodzi mwa malamulo ochepa amene sanabwezeretsedwe mu Chipangano Chatsopano. Kusunga kwa lamuloli kumachitika mwa Mwambo ndi mwa kuthupi ndipo kunayala maziko a madalitso a mpumulo wa Sabata lenileni limene linali kubwera mwa Yesu Khristu.

Pali anthu ambiri padziko lino amene amakakamira Lamulo la Sabata. Iwo amakhulupirira kuti kupembedza pa tsiku Loweruka ndi chimene Mulungu amafuna chidzichitika. Tsoka ilo, zoonza zake ndizo zakuti iwowo amasemphana ndi tanthauzo loona la Sabata lenileni. Magulu achipembedzo ambiri amachimwa komanso kukhala mu moyo wosamvera Mau a Mulungu, komabe iwo amapeza chitetezo chawo mu kusunga Sabata. Sitalinso pansi pa ulamuliro wa Chipangano Chakale ndipo tili ndi muyezo waukulu wa chiyero ndi mpumulo kusiyanana ndi uwo umene unaperekedwa ndi mpumulo wathupi komanso kupembedza pa Sabata.

Phunziro lofunikira koposa tikhoza kulipeza pamene tikulingalira za iwo amene mpaka lero amasungabe Sabata. Pali kusiyanana kwaukulu pakati pa a Seventh Day amene amadzinena kuti amasunga Malamulo a Mulungu. Chipangano Chakale sichingophunzitsa kokha za kupereka nsembe ndi nsembe zopsezera, koma chimaphunzitsanso za kusunga masiku azikondwerero zambiri kukhala wopatulika kwa Ambuye. Kugwirizana kwake kuli pati pamenepa? Ponena za Sabata, Chipangano Chakale chimaphunzitsa kuti ana a Israele samayenera kuchoka “pamalo awo” pa tsiku la Sabata. Panali chilango cha Imfa kwa aliynse amene anapezeka akugwira ntchito pa Sabata. Kodi okhulupirira a Seventh Day amatsatiradi zimenezi? Ichi ndi chifukwa chake kuli koyenera kuti tisangotola ndi kusankha zimene tikufuna kuti tiphunzitse zochokera mu Chipangano Chakale. Pamene timaphunzira zambiri kuchokera ku Chipangano chakale, tizindikire kuti pansi pa Chipangano Chatsopano tili ndi chazimu chokoma ndi chokwanira chimene tiyenera kuchichita.

Ngakhale kuti mu nyengo ino tili ndi ufulu wa kugwira ntchito ndiponso ufulu wa kupembedza, mdaniyo watengerapo mwayi. Anthu ambiri pakati pa oyera mtima akumatanganidwa kwambiri mwakuti akumakanika kupeza mpata wokapembedza pamodzi ndi anzawo. Kupita kukapembedza chimakhala chinthu chochitika mothamanga potengera kuti tsikulo lili ndi ntchito zotani. Nkofunikira kwambiri kuti tisayiwale maphunziro enieni okhudza kupumula ndi kupembedza zimene tinaphunzitsidwa mu Chipangano Chakale.

Chinanso chofunikiranso kwambiri, tiyeni tiyesetse kuti tilowe mu mpumulo weniweni wamoyo umene upezeka mwa Khristu pamene tikuyesetsa kudzichepetsa tokha ndi kupeza chitetezo mu chilungamo cha Mulungu.

Michael W. Smith

April 2017

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti muone

makalata akale.

Kalozera Posanthula Mau a Mulungu: Sabata

Kuwerenga Malemba: *Chifukwa chake munthu aliyense asakuweruzeni inu m'chakudya, kapena chakumwa, kapena m'kunena tsiku la chikondwerero, kapena tsiku lokhala mwezi, kapena la Sabata; ndizo mthunzi wa zilinkudzazo; koma thupi ndi la Khristu.* —Akolose 2:16-17

Mwachidule: Kusunga Sabata chinali chinthu choyenera kuchichita mu Chipangano Chakale. Mwambo uwu wosunga tsiku limodzi kuti likhale lopatulika kwa Mulungu unakwaniritsidwa mu Chipangano Chatsopano kudzera mwa Yesu Khristu. Yesu amapereka mpumulo weniweni wa moyo ndipo mwana wa Mulungu ayenera kusunga tsiku lililonse ngati lopatulika kwa Ambuye.

I. Kukhazikitsa kwa Sabata la Mose

- A. Eksodo 16:22-30 Loyamba linakhazikitsidwa.
- B. Eksodo 20:8-11 Lamulo linaperekedwa pa Phiri la Sinai.

II. Sabata silinatsatidwe mpaka nthawi ya Mose

- A. Nehemiya 9:14 Linadziwitsidwa ndi Mose.
- B. Duteronomo 5:15 Linalamulidwa anthu atamasulidwa kuchokera ku Ejipito.

III. Zifukwa za Sabata

- A. Eksodo 23:12 Mpumulo.
- B. Eksodo 20:11 Kumbukirani Mlengi kapena chilengedwe.
- C. Duteronomo 5:12-15 Kumbukirani kuombedwa kuchokera ku Ejipito.
- D. Levitiko 23:3-8; (19:30) Nthawi ya kupembedza.

IV. Lamulo lolembedwa la Sabata

- A. Eksodo 31:12-17 (35:2-3) Imfa kwa aliyense wogwira ntchito.
- B. Numeri 15:32-36 Munthu wotola nkhuu agendedwa.
- C. Nehemiya 13:17-19 Yuda anyozetsa Sabata.
- D. Lamulo linali pangano kwa anthu a Chiyuda
- E. Eksodo 31:17 Chizindikiro pakati pa Mulungu ndi ana a Israele.

VI. Lamulo la Chipangano Chakale silikugwiranso ntchito (Onani Kalata ya No. 18)

- A. Ahebri 8:8-9, 13 Lamulo la Mose siligwiranso ntchito (Yeremiya 31:31-32).
- B. Luka 16:16 Lamulo linalipo mpaka nthawi ya Yohane Mbatizi.
- C. Agalatiya 3:11-13 Palibe munthu amalungamitsidwa ndi Lamulo.
- D. Aroma 6:14 Osati pansi pa Lamulo (Aroma 7:6).
- E. Machitidwe 15:5, 24, 28-29 Kusunga Lamulo la Mose sikulamulidwa.

VII. Yesu ndiponso Sabata

- A. Mateyu 12:1-8 Yesu anavomereza kuthyola tirigu ndi kumadya.
- B. Marko 2:27 Yesu ndiye Mbuye wa Sabata.
- C. Mateyu 12:9-14 Lamulo limavomereza kuchita ntchito zabwino pa Sabata. (Yohane 5:8, 9)

VIII. Sabata la Chikhristu

- A. Ahebri 10:1 Lamulo linali chithunzithunzi cha zinthu zabwino zilinkudza.
- B. Mateyu 5:17 Yesu anakwaniritsa Lamulo.

- C. Yesaya 11:10 Kulosera za Mpumulo waulemerero.
- D. Ahebri 4:1-11 Mpumulo weniweni wa Sabata uli mwa Khristu.
- E. Mateyu 11:28 Yesu ndiye wopereka mpumulo wauzimu.
- F. Akolose 2:16-17 Munthu aliyense asaweruze mokhudzana ndi tsiku la Sabata kapena masiku ena opatulika.
- G. Luka 1:74-75 Tsiku lililonse ndi loyera.

IX. Tsiku la Ambuye: Tsiku la chikhristu lopembedza kuyambira kale

- A. Chivumbulutso 1:10 Tsiku la Ambuye.
- B. Luka 24:1 (Mateyu 28:1) Khristu anaukitsidwa pa tsiku loyamba la sabata.
- C. Machitidwe 2:1 Tsiku la Pentekoste linali Lamulungu.
- D. I Akorinto 16:1-2 (Machitidwe 20:7) Otsatira Khristu amapembedza tsiku Lamulungu.

Kumaliza: *Koma tsopano, podziwa Mulungu inu, koma makamaka podziwika ndi Mulungu, mubwereranso bwanji kutsata miyambo yofooka ndi yaumphawi, imene mufuna kubwerezanso kuichitira ukapolo? Musunga masiku, ndi miyezi, ndi nyengo, ndi zaka.*

Agalatiya 4:9-10

NJIRA ZINAYI ZIMENE MALAMULO ABWINO AKHOZA KUSIYA KUGWIRA NTCHITO

(Kuchokera ku zolemba za Adam Clarke)

1. Pogwiritsa ntchito Lamulo la chilengedwe la kufunikira.
2. Pogwiritsa ntchito Lamulo, limene lili pamwamba.
3. Pogwiritsa ntchito Lamulo la chikondi ndi chifundo.
4. Pogwiritsa ntchito nyengo ndi ulamuliro wa wopereka lamulo.

Nkhani izi zili ndi zitsanzo zake mu
Mateyu 12:4-8.

Sabata

“Udzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika.” (Eksodo 20:8). Lamulo lachinai linakhazikitsidwa ndi Mulungu pamene Iye anapereka Malamulo Khumi pa Phiri la Sinai. Ilo linapatula Loweruka, limene lili tsiku lomaliza la sabata, kuti likhale tsiku lopatulika la kupembedza mu nthawi ya Chipangano Chakale. Anthu a Mulungu amayenera kugwira ntchito kwa masiku asanu ndi limodzi koma tsiku la chisanu ndi chiwiri linaikidwa ndi Mulungu kuti ndilo tsiku lopuma ndi losayenera kuti wina agwire ntchito.



“Ngakhale kuti Mulungu anapuma pa tsiku lasabata atalenga dziko...tsikuli silinayeretsedwe kufikira patapita nthawi ndithu.”

Chiyambi cha Sabata

Nthawi yoyamba imene ikudziwika bwino kuti anthu anasunga Sabata kukhala tsiku lopumula ndi pamene Mulungu anatumiza mana kuti adyetse ana a Israele mu chipululu pamene iwo amachoka ku ukapolo wa ku Ejipito. Anthuwo anatola buledi wochuluka kawiri pa tsiku lachisanu, chifukwa Mulungu sanatumize mana pa tsiku Loweruka, popeza linali la “kupuma, Sabata lopatulika la Yehova” (Eksodo 16:22-30). Kusunga Sabata kotereku posakhalitsa kunalimbikitsidwa ndi chipangano cha Mulungu cha Malamulo Khumi pamene anadalitsa ndi kupatula tsiku la Sabata (Eksodo 20:11).

Silinasungidwe Mose asanabwere

Sitimvako mu mbiri kapena mu zolemba zakuti makolo athu oyamba aja ankasunga Sabata nthawi imene Lamulo la Mose linali lisanakhazikitsidwe. Panadutsa zaka zoposera 2,500 Mose anasabwere ndipo mu nthawi yonse yalibe umboni wogwirika bwino wakuti Sabata limasungidwa kapena kulemekezidwa. Nawa ndi Abrahamu anayenda mwa chikhulupiriro ndipo anapeza chisomo pamaso pa Mulungu koma sanasunge tsiku Loweruka kukhala tsiku lopatulika. Ngakhale kuti Mulungu mwini anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri atatha kulenga dziko (Genesis 2:3), panapita nthawi yaitali ndithu kuti tsikuli liyeretsedwe. Sabata lopatulika linadziwika kwa ana a Israele monga “mwa dzanja la Mose” (Nehemiya 9:14) ndipo linalamulidwa ana a Israele atachoka ku dziko la Ejipito (Duteronomo 5:12-15).

Cholinga cha Sabata

Sabata, kapena Kupumula, linali tsiku limene Mulungu anakhazikitsa mu Chipangano Chakale pa zifukwa komanso zolinga zingapo.

Limayenera kukhala tsiku lopumula ndi kutsitsimuka kwa munthu ndi nyama yomwe. “Uzichita ntchito yako masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri uzipumula; kuti ng’ombe yako ndi bulu wako zipumule, ndi kuti mwana wa mdzakazi wako ndi mlendo atsitsimuke” (Eksodo 23:12). Linali tsiku makamaka lokumbukira Namalenga wa dziko lonse lapansi (Eksodo 20:11); linalinso tsiku la chikumbutso kwa ana a Israele ndipo anawauza kuti “Ndipo uzikumbukira kuti unali kapolo m’dziko la Ejipito, ndi kuti Yehova Mulungu wako anakutulutsako...” (Duteronomo 5:15). Sabata linali nthawi yoikidwa padera kuti apembedze mu hema lokomanamo. Pa tsiku losagwira ntchitoli, panali kukhala “kukumana pamodzi kwa oyera” kapena msonkhano wa iwo amene akupembedza Yehova (Levitiko 23:3-8).

Lamulo Loopsa

Kwa Ayuda, kusunga Sabata sichinali chiganizo chabe cha Mulungu, koma linali lamulo lomveka bwino ndi lalikulu, choncho chilango cha lamulo lokhudza Sabata chinali choopsa. Limayenera kusungidwa kuti likhale lopatulika ndipo “aliyense wakuliipsa aphedwe ndithu...aliyense wogwira ntchito tsiku la Sabata aphedwe ndithu” (Eksodo 31:14-15). Pa gawo lina, chilango chowawachi chinaperekedwa ndi Mulungu chifukwa ana a Israele anali kumanga hema lokomanako. Tsono Iye sanafune kuti iwowo akhale otanganidwa ndi kugwira ntchito imeneyi mpaka kufika poyiwala kusunga Sabata. Ana a Israele analetsedwa kuyatsa moto ndi cholinga chakuti agwire nawo ntchito kapena aphikire (Eksodo 35:2-3). Ayudawo amamvetsetsa kuti akhoza kusunga moto kuti awunikire kapena kuti atenthedwe. Pamene anali mu chipululu, ana a Israele anapeza munthu akutola nkhu pa Sabata. Munthuyo anabwera naye kwa Mose ndi Aroni. Yehova anauza Mose kuti munthuyo aphedwe poponyedwa miyala kunja kwa mudzi, ndipo zinachitikadi (Numeri 15:32-36). Uchimo wake unali wakuti iye sanachita izi mwa kusadziwa, koma kuti anaswa mwadala chilamulo cha Mulungu. Lingalirani za kuopsa kwa Mulungu.

Sabata Linyozedwa

Mu zaka zakutsogolo, akuluakulu a Ayuda anadetsa tsiku la Sabata. Zipata za ku Yerusalemu zinasidiyidwa zotsegula kuti amalonda ndi apaulendo alowe (Nehemiya 13:17-19). Nehemiya adalamulira kuti zipata za mzindawo zitsekedwe pofuna kuletsa kuchita malonda pa Sabata. Amalonda aja adamanga zisakasa zawo kunja kwa mzindawo mpakana bwanankubwa uja analetsanso zimenezi pofunitsitsa ndithu kuti

(Yapitirira pa tsamba 6)

ayeretse tsiku la Sabata. Pamene anthu anasiya kusunga Sabata, iwo anasiyanso kupembedza Mulungu ndipo uchimo unachuluka kwambiri. Kugwira ntchito pofuna kupeza phindu la kuthupi kumaletsedwa pa tsiku lopatulikali mu nthawi iyi ya Chilamulo. Poyika Sabata, cholinga chinali chakuti lisatipatse ukapolo koma likhale tsiku la chimwemwe,

kupumula, kuchita chifundo, kukumbukira ndiponso kupembedza.

Ndi la ku Chipangano Chakale

Lamulo la Sabata limagwira ntchito kufikira pamene panganolo linasinthidwa ndipo m'malo mwake panabwera njira yatsopano ndi yamoyo. Monga ananenera pa Yeremiya 31:31-32 ndi kudzabwerezanso pa Ahebri 8:8-9, 13:

“Taonani, akudza masiku, anena Ambuye, Ndipo ndidzapangana pangano latsopano ndi nyumba ya Israele, ndi nyumba ya Yuda, losati longa pangano ndinalichita ndi makolo ao. ...Pakunena Iye, Latsopano, anagugitsa loyambali. Koma chimene

chilinkuguga ndi kusukuluka, chayandikira kukanganuka.”

Khristu anabweretsa Mpumulo wa Moyo

Ndi kubwera kwa Yesu Khristu, chilamulo cha Chipangano Chakale sichikhalanso ndi ntchito. “Chifukwa chilamulo chinapatsidwa mwa Mose; chisomo ndi choonadi zinadza mwa Yesu Khristu” (Yohane 1:17). Anthu sanakhalsenso pansi pa nsinga za chilamulo koma ndi afulu wa uzimu, “popeza simuli a lamulo koma a chisomo.” (Aroma 6:14). Pansi pa Chipangano Chakale, Ayuda amalungamitsidwa kudzera mu miyambo yakuthupi komanso kusunga zolamulidwa. Mu nyengo ya Chipangano Chatsopano, anthu amalungamitsidwa mwachisomo pokhulupirira mwa Khristu. “Pakuti onse amene atama ntchito za lamulo liwakhallira temberero...palibe munthu ayesedwa wolungama ndi lamulo pamaso pa Mulungu...Khristu anatiombola ku temberero la chilamulo” (Agalatiya 3:10-13). Kusunga Sabata sikunabwerezedwe mu Chipangano Chatsopano (Machitidwe 15:5, 24-29) ndipo ana a Mulungu amakhala omasulidwa ku ukapolo umenewo.

Sabata silikubwerezedwa ndi Khristu

Mu chiphunzitso za Khristu, Iye sanabwereze Lamulo la Sabata, ngakhale pamene anabwereza ena mwa Malamulo (Marko 10:19). Iye anadzudzulidwa ndi Afarisi pamene analola ophunzira ake kuti adzitola tirigu ndi kumadya (Mateyu 12:1). Yesu anachiritsa pa Sabata ndipo potero anatsimikiza zochita ntchito zabwino pa tsiku ngati ili (Mateyu 12:9-14). Iye analamulira munthu amene amadwala kuti ayalule mphasa yake ndi kuyenda pa tsiku la Sabata

(Yohane 5:8-11). Yesu ponena za zinthu izi anati: “Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha Sabata” (Marko 2:27). Khristu, monga mkhalapakati komanso mwana wa Mulungu, anali ndi ulamuliro wophwasula ndi kusintha zokhudza kasungidwe ka tsikulo.

Kukangamira ku Lamulo Lakale

Lero anthu ambiri akugwiritsitsa pa chiphunzitso cha kusunga Sabata kukhala lopatulika. Malemba amaphunzitsa mwomveka bwino kuti anthu a Mulungu salinso pansi pa Lamulo. “Koma tsopano, podziwa Mulungu inu... mubwereranso bwanji kutsata miyambo yofooka ndi yaumphawi, imene mufuna kubwerezanso kuichitira ukapolo? Musunga masiku, ndi miyezi, ndi nyengo, ndi zaka” (Agalatiya 4:9-10). Mau a Mulungu amapitiriza kutiphunzitsa kuti munthu aliyense asaweruze “m’chakudya, kapena chakumwa, kapena m’kunena tsiku la chikondwerero, kapena tsiku lokhala mwezi, kapena la Sabata; ndizo mthunzi wa zilinkudzazo” (Akolose 2:16-17).

Khristu Ndiye Sabata Lathu

Kusunga Sabata sichinali chinthu chimene chimachitika chifukwa chinali chabwino koma chifukwa chimayenera kuti chidzitsatiridwa. Mu Chipangano Chatsopano, kupereka nsembe, miyambo, zofukiza, ndi kupembedza mu kachisi ndi zina zotere zinadutsa ndipo zakwaniritsidwa mwa Yesu Khristu. Kusunga kwa Sabata ngati tsiku la mpumulo lopatulika unali mtundu wa mpumulo wodabwitsa ndi wauzimu umene upezeka mwa Yesu Khristu. Khristu ndiye Sabata lathu ndipo Mpumulo wake umaposa kwambiri tsiku limodzi la Sabata lakupuma kuthupi ndi kupembedza. Ahebri 4:1-11 akunena modabwitsa za choonadi cha mpumulo weniweni wa anthu a Mulungu amene amasiya ntchito zawo zathupi kuti alungamitsidwe pamaso pa Mulungu ndipo mwachikhulupiriro amalowa mu mpumulo wa Mulungu. Kusunga Sabata kwenikeni kunali ngati chithunzithunzi chabe cha mpumulo waulemerero, wosatha ndi wauzimu mu nyengo ino ya chisomo, ndi chifukwa chake Khristu akuitana anthu onse kuti: “Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi kuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumultsani inu” (Mateyu 11:28).

Mpumulo wa Miyoyo yathu wa Sabata lenileni

Kusunga kwa tsiku lopatulika kwa kuthupi ndi cholinga chakuti apembedze Mulungu kunatipatsa mphamvu komanso kuthekera kuti tsiku lililonse tikhoza kukhala mmoyo wachiyero kudzera mwa Khristu. “Kutipatsa ife kuti titalanditsidwa kudzanja la adani athu, tidzamtumikira Iye, opanda mantha, m’chiyero ndi chilungamo pamaso pake, masiku athu onse” (Luka 1:74-75).

Sabata ya Chikristu yeniyeni mu nthawi ya Chipangano Chatsopano ndiyo ya mtendere, mpumulo, kupembedza kwa uzimu, ndiponso kukhala moyo wachiyero tsiku lililonse la sabatalo. Tsiku lililonse ndi lopatulika ndiponso lisungidwe kukhala lolingalira ndiponso kukumbukira kuombedwa ku uchimo kudzera mwa Yesu Khristu. Tiyamika Mulungu chifukwa kuti tikhoza kukondwera chifukwa cha Sabata!



Kodi ndi chifukwa chiyani Malemba akunena kuti Sabata lidzisungidwa kwa mibadwo yonse?

Pa Eksodo 31:16-17 amanena kuti, “Chifukwa chake ana a Israele azisunga Sabata, kuchita Sabata mwa mibadwo yao, likhale pangano losatha; ndicho chizindikiro chosatha pakati pa Ine ndi ana a Israele...”

Lamulo la Sabata linali chizindikiro pakati pa Mulungu ndi mtundu wa Ayuda. Ilo linali la iwo okha ndipo linali ngati lamulo la dziko. Ilo linayenera kusungidwa mpaka kalekale monga m’mene amachitira ndi mdulidwe, sabata la mkate woonekera, unsembe wa Alevi ndi zina zotere. Kwa nthawi zonse sikutanthauza kuti mpaka muyaya. Lamulo la Sabata, monga m’mene ilili miyambo ina ya mu Chipangano Chakale, limayenera kusungidwa ngati lamulo lokhazikika ndiponso loyenera kutsatidwa mpakana nthawi imene lamulo lina latsopano lidzalowe m’malo mwake. Machitidwe oterewa amayenera kupitirira kutsatidwa mpakana ena osinthana nawo atabwera. Sabata linakwaniritsidwa mwa Khristu amene tsopano ali mpumulo wathu wamuyaya, mu mpumulo wa Sabata limene likupitirira. Lamulo limene linasiyanitsa Ayuda ndi amitundu linathetsedwa pa mtanda wa Khristu (Aefeso 2:11-18).

Kodi ndi kolakwika kugwira ntchito tsiku Lamulungu?

Sitilinsu pansu pa Lamulo la Sabata pamene kunali koletsedwa kugwira ntchito ya mtundu uliwonse. Ngakhale kuti Akhristu amapembedza pa tsiku Lamulungu, zolamulira za Lamulo la Sabata sizinapitirire kuti zikagwirensu ntchito mu Lamulungu pansu pa Pangano Latsopano.

Ngakhale tanena zimenezi, tiyeni tikumbukire kuti “Momwemo chilamulo chidakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Khristu” (Agalatiya 3:24-25). Ngakhale kuti pano sitilinsu pansu pa namkungwi, kukhoza kukhala kupusa ngati tiyiwala zophunzitsa zimene zili pansu pa Lamulo. Chimodzi cha zifukwa zimene Sabata lidakhazikitsidwa kunali kupereka tsiku lopumula kwa munthu ndi nyama kuti akamayambiranso kugwira ntchito sabata linali akhale atapumula kuthupi ndi kuuzimu. Ngakhale kuti palibe lamulo la tsiku Lamulungu, pali mfundo ina imene ili yofunikira kwambiri. Mpumulo ndi wofunika ndipo anthu

amachita bwino pa zinthu zambiri ngati akhala ndi tsiku limodzi lopumula ku ntchito zawo kuti akhale ndi nthawi yopembedza komanso kukhala ndi banja lawo.

Nthawi zambiri anthu akugwiritsa ntchito “ufulu wanu chothandizira thupi” (Agalatiya 5:13) ndipo tsiku Lamulungu limangokhala ngati tsiku lina lililonse. Anthu akugwira ntchito kwambiri ndipo ndi otanganidwa ndi zosamalira za moyo uno. Kupembedza kwa tsiku Lamulungu kumangokhala chinthu chimene anthu amachita mongothamanga ndi mofulumira kuti basi amalaze kenaka nkumapita kukagwira ntchito.

Anthu oyera mtima a Mulungu amayenera kupatula nthawi kupembedza ndi okhulupirira anzao ndipo asamalolere kuti zotanganidwitsa za moyo uno zisokoneze zinthu zimene zili zofunikira kwambiri. Ngakhale kuti sindife anthu osunga Sabata ndipo siti yenera kukhala pansu Lamulo, pali nzeru komanso kupindula ku uzimu pamene tisunga tsiku lathu lopembedza ndi kuti lisaphatikizane ndi zinthu zina zimene timazichita tsiku lililonse.

—mws

Sabata la Mose *ndi* Sabata la Chikhristu

La Mwambo	La Uzimu
Mpumulo wa ku thupi	Mpumulo wa ku uzimu
Tsiku lachisanu ndi chiwiri likhale	Tsiku lililonse likhale lopatulika
Kugwira ntchito yamanja kumadetsa tsikuli	Kugwira ntchito kapena kusagwira ntchito sikudetsa kapena kuyeretsa tsikuli
Aliyense samayenera kugwira ntchito yamanja	Aliyense adziletse ku ntchito zonse zauchimo
Kugwira ntchito pa Sabata kumabweretsa chilango cha Imfa	Kuchita uchimo kumaononga mpumulo wa mzimu ndipo kumabweretsa imfa ya uzimu
Mdalitso wosakhalitsa	Mdalitso wauzimu
Chizindikiro ndi Chithunzithunzi	Kukwaniritsidwa



KODI MUKUDZIWA?

Zimene ananena Akhristu ena a mu Mpingo Woyamba

Mu Lamulo latsopano anthu amayenera kusunga Sabata mpaka kalekale. Komabe chifukwa choti sunagwire ntchito kwa tsiku limodzi, nanga kapena ndiwe wolungama —Justin Martyr, 160 AD

Anthu onse olungama amene atchulidwa kale [Adamu, Abele, Enoke, Loti, Melkizedeke], ngakhale sanasungepo Sabata, koma anakondweretsa Mulungu.

—Justin Martyr, 160 AD

Monga unathetsedwera mdulidwe wa ku thupi ndiponso lamulo lakale limanetsa kuti linafika pamapeto pa nthawi zina ndi zina, chonchonso kusunga Sabata kukuoneka kuti sikunali kwamuyaya. —Tertullian, 197 AD



A Word
In Season

Mukhalebe Olumikizana ndi Khristu

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
PO Box 2042
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.org

Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala chipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine —Yohane 15:4

Utumiki waphindu umalira nthawi ndi kudzipereka. Umapangitsa kuti thupi litope komanso lisiye kuchita zinthu zina. Atatumikira kwa zaka zochuluka, munthu aliyense ngakhale akhale wanzeru kapena wodziwa ntchito akhoza kumasulira malemba komanso kuonetsa ngati ndi wachilungamo. Ngakhalebe ena akhoza kumadalitsika, kudzoza komanso moto wa Mzimu kukhoza kumasowa ndipo utumiki ukhoza kukhala ntchito yolimba ndi yotopetsa.

Utumiki wopindulitsa umadza osati kuchokera ku kuthekera kwa kuthupi kokha ai, koma kuchokera mu chipatso chimene chimakula pamene munthuyo ali pa ubale ndi Yesu Khristu. Yesu analangiza ophunzira ake kuti “Khalani mwa Ine”—mukhazikike mwa Ine, mudzikhala ndi Ine, yendani ndi Ine. Kapena kunena kwina, mukhale olumikizana ndi Ine.

Ndi koyenera ndi kofunikira kuti atumiki a Ambuye ndi anthu onse a Mulungu asamalitse pamene akutumikira anthu ena komanso kukwaniritsa utumiki wolalikira uthenga wabwino ku dziko lonse kuti pamene akuchita izi asatayane ndi Khristu. Mdaniyo amagwiritsa ntchito zinthu zovomerezeka ndi lamulo ngakhaleenso zinthu zabwino za moyo uno pofuna kusokoneza kulumikizana kwathu komanso umodzi wathu ndi Mzimu kuti potero afooketse kulumikizana kwa anthu ndi Mulungu.

Pamene zokhoma ndiponso kutopa mu utumiki zifika ndi kukhazikika pa thupi lanu, senderani kwa Mulungu. Khalani ndi nthawi panokha yomufunafuna Ambuye komanso kudzilumikizitsa nokha kwa Iye. Ngati chikho chanu chili chodzadzaza, pamenepo mukhoza kutumikira anthu ena ndi mphamvu komanso kudzoza popeza panokha mwalumikizana ndi Khristu.

—mws



CHIYERO CHA KWA AMBUYE